# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NKHATA BAY M'DZINJA LA 2024-2025

# DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi LaNina. La Nina ndi kuzizira koposera mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific.
Madera ambiri m'bomali akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera mlingo okhazikika. Ngakhale zili chonchi, mvula idzachepera mlingo okhazikika mu mwezi wa November.

## October 2024





Nyengo yotentha ndi yopanda mvula ikuyembekezeka mwezi wa October. Komabe, Ulosi ukuonetsa kuti m'madera ena adzalandira mvula ya Chizimalupysa

## November 2024





Mvula yochepera mlingo okhazikika ikuyembekeseka mwezi wa November. Madera ambiri kudzakhala nyengo yotentha ndi yoppanda mvula. Komabe mvula ya chizimalupysa ingadzagwe m'madera ena, yomwe idzatsatane ndi mphepo ya mkhuto, ziphaliwali ndi mabingu. Mvula ya chizimalupysayi idzagwe yochulukirapo m'madera ena ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 100mm.

## December 2024





Mu December, madera ambiri m'bomali adzalandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera apo yomwe mlingo wake udzakhala wapakati pa 150mm ndi 200mm. Madera ena monga kwa TA Timbiri ndi SC Malanda adzalandira mvula yosachepera mlingo wa 250mm.

## January 2025





Mvula yochuluka ikuyembekezeka madera ambiri mwezi wa January. Madera ambiri monga kwa TA Fukamapiri, TA Timbiri, TA Kabunduli, ndi TA Boghoyo akuyembekezeka kulandira mvula yoposera mlingo wa 250mm.

## February 2025





Mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposa mlingowu ikuyemebekezeka madera ambiri. Mvula ya mlingo wa mpakati pa 150mm ndi 200mm ndi yomwe ikuyembekezeka m'madera monga TA Malenga Mzoma, SC Nyaluwanga, ndi TA Mankhambi. Mvula ya mlingo oposera 200mm idagwa madera ena monga kwa SC Zilakoma.

## March 2025




Mvula ikuyembekezeka kupitilira madera ambiri.
Mvula yochuluka idzagwa madera akufupi ndi Nyanja monga ozungulira pa Boma komanso kwa SC Malanda.


## April 2025




Mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposa, yomwe ndi ya mlingo wa pakati pa 100mm ndi 150mm ndi yomwe idzagwa madera ambiri mwezi wa April. Madera ena akufupi ndi Nyanja adzalandira kuposera mlingo wa 250mm.

- Mvula yodzalira idzachedwerapo, ndipo ikuyembekezeka pakati pa sabata ya chitatu ndi yachinayi mwezi wa December 2024.
- Dzinja likuyembekezeka kufika kumapeto sabata ya chinayi ya mwezi wa April m'madera ambiri.
- Dzinja likuyembekezeka kukhala yotalika masiku 120 ndi 150, koma madera ena ndi ena masiku ochepera 120
- Chiopsezo cha ng'amba ndi chochepa. Ng'amba ya sabata imodzi ndi yomwe ikuyembekezeka mu January ndi February

| NKHATABAY | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.3 | 10.7 | 12.5 |
| NOV | 23.0 | 93.1 | 72.0 |
| DEC | 139.0 | 232.7 | 214.8 |
| JAN | 162.8 | 243.5 | 215.9 |
| FEB | 149.2 | 242.2 | 228.6 |
| MAR | 255.0 | 308.2 | 341.8 |
| APR | 243.2 | 362.9 | 289.1 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**


**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com